

Ana a mileme

Zomwe tiphunzira sabata ino:

- Chifukwa chiyani ndizovuta kwambiri kukhala mleme wamayi
- Ndi chisa chotani nanga
- Zomwe zimapanga chisa cha amayi abwino
- Mleme wamng'ono ayenera kuphunzira kuti apulumuke

Phunziro
5



Wawa, ndine Spike. Phunziroli ndi lokhudza ana a mileme, koma popeza ndine wamwamuna sichinthu chomwe ndimachidziwisitsa. Mileme yachibambo sathandiza kusamalira ana mileme. Kotero ndikupereka nkhaniyi kwa akatswiri



Moni, ndine Saba, mutha kundidziwa ngati 'Dinagn's bat', 'African yellow bat', a 'yellow bellied house bat' kapena 'African yellow house bat'. Ndili ndi ana amapasa, amandiyitana kuti "amayii"!



Moni ndine Bongi. Ndine a 'Botswanan brown long-eared bat', Ndine mayi wonyadira kwambiri wa mwana wanga Logan. Kusamalira mwana mmodzi ndi ntchito yovuta kwambiri, sindikudziwa kuti Saba amakwanitsa bwanji ndi awiri.

Musaiwale, chizindikiro cha pensulo chimatanthauza kuti ndi nthawi yanu yoti muchitepo kanthu!

Taphatikiza mawu onse atsopano pamndandanda wamawu kumapeto!



Mudzafunika:

✓ pensulo

✓ chowerengera



1

Amayi a mileme ndi abwino koposa!

Kumapeto kwa masika, pomwe usiku umayamba kutentha ndipo chakudya chimakakhala chokwanira, mileme yoyamwitsa imayamba kukonzekera kubereka ana. Choyamba ayenera kupeza malo otentha, otetezeka oti azigonamo, makamaka malo omwe chakudya chimapezeka chabwino. Awa amakhala malo omwe amabelekelamo.

Awa ndi malo omwe adzikhalamo;

- pamene ali ndi mimba,
- kumeneko adzabereka ana
- kumene amasamalira mwana awo mpaka atakula n'kuyamba kuuluka, n'kuyamba kudzipezera chakudya ndiponso kukhala opanda azimayi awo.



2

Malo obelekelamo ana




Malo omwe mileme yoyamwitsa ndi ana awo amatchedwa malo obelekelamo. Mileme yaikazi ikapeza malo abwino okhala, amayesesa kubwererako chaka chilichonse kuti azikabereko ana awo wotsatira.

Mleme wamkazi umabwerera kumalo kumene unabadwira pamene ukuyembekezera mwana wake (ngati malawo akadalipo). Ndizotheka kuti amakapezako amayi ake, agogo ake aakazi ndi azakhali ake ambiri atabwereranso kumalo ubalekelaku, aliyense akuyembekezersanso mwana.

Ngati malo obelekelamo awonongeka, mwachitsanzo ngati mtengo wagwa, nyumbayo yagwetsedwa kapena phanga labata mwalowa phokoso chifukwa cha zokopa alendo, mileme yoyembekezela iyenera kupeza malo atsopano. Kupeza malo omwe ali ndi zonse zoyenera, (ofunda bwino, yotetezeka komanso pafupi ndi chakudya) kumakhala kovuta ndipo kumanangitsa moyo kukhala wovuta kwambiri kwa mileme yapakati.

Malo obelekelawa amakhala ndi azimayi oyembekezera komanso (mileme yayikulu nsikhu) ana aamuna ndi aakazi / mileme yaing'ono. Amuna akuluakulu sathandiza kusamalira ana ndipo amakhala m'malo osiyana.


Kwa inu!



Ntchito 1:

Kodi mungawerenge amayi ndi ana a mileme angati pachithunzichi?

Nkati mwamtengowu muli amayi ambiri ndi ana awo, akumakumbatirana kuti akhale ofunda. Ndi amayi angati (maso akulu) ndi ana angati (maso aang'ono) omwe mungawerenge?



Mileme yaing'ono (monga Bongi ndi Saba) kawirikawiri imakhala ndi pakati kwa masabata 6 mpaka 9. Imeneyi ndi nthawi yayitali kwa nyama yaing'ono ngati imeneyi. (Mbewa nthawi zambiri imakhala ndi pakati kwa masabata atatu.)

Nthawi imene nyama imakhala ndi pakati imatchedwa nthawi ya bere. Mleme wachikazi wamkulu wokhala ndi thanzi labwino nthawi zambiri amakhala ndi mwana mmodzi pachaka. Mitundu ina ya mileme imakhala ndi mapasa, koma imeneyi ndi yapadera. Mitundu yambiri imakhala ndi mwana mmodzi yekha.



Ndinadziwa kuti ndine wapadera. Kukhala ndi mapasa ndi chinthu chopambana

mwana mmodzi mmodzi yokwanira kwa ine!



Koma sitili ngati nyama zina zoyamwitsa zinzathu, mbewa, zomwe zimabereka ana ambiri kangapo pachaka! Ayi zikomo!!



Iyenera kukhala ntchito yovuta kwambiri kuti mileme ibereke. Mwana akabadwa amakhala wamkulu kwambiri poyerekeza ndi kukula kwa mayi ake.




"Logan anali 2.5 magalamu pamene anabadwa, sizingamveke zambiri kwa inu koma ndinangolemera magalamu 7 ndisanakhale ndi pakati. Iye anali akupitirira gawo limodzi mwa magawo atatu a kulemera kwanga kwanthawi zonse!"

"Ndinali ndi magalamu 50 pamene ndinabadwa, chimenecho chinali pafupifupi gawo limodzi mwa magawo asanu ndi limodzi a kulemera kwake kwa amayi anga (300 magalamu). Pamene ndinasiya kuyamwa ndinali nditalemera magalamu 135."



Kwa inu!



Ntchito 2: Kulemera kwa mwana


Mungakonde kudziwa gawo la kulemera kwa amayi anu pomwe munabadwa.

Kuti muchite izi gawani kulemera kwa amayi anu (asanakhale ndi pakati) ndi kulemera kwanu pamene munabadwa. (ndibwino mugwiritse ntchito ma kilogramu osati mapaundi). Kenako ikani yankho lanu pansu pa 1 mwachitsanzo ngati kulemera kwa amayi kugawidwa ndi kulemera kwa mwana = 19, chigawocho ndi 1\19th.

Ngati amayi anu sakukumbukira nachi chitsanzo:

Kulemera kwa amayi asanatenge mimba = 60Kg
Kulemera kwa mwana pakubadwa = 3kg

Yankho:




5 Tapilila Mwana!

Ana a mileme akabadwa amakhala osazidalila okha, maso awo samapenya, amakhala opanda ubweya koma nthawi yomweyo amadziwa kuti ayenela kudalila amayi awo. Ama gwiritsa ku nsonga la bere ndi kamwa yake ndi kuwafumbatila thupi lawo ndi zala zake. Akakhala chonchi amadyetsedwa, kutenthedwa ndi kukumbatidwa bwino.



6 Kudyetsadwa ndi kuwuluka



Poyamba, amayi ndi mwana amakhala nthawi zonse limodzi. Mwana amamwa mkaka wa mayi ake. Mayi ayenera kumadzidyetsa bwino kuti apange mkaka wochuluka wa mwana wawo akulela. Izi zikutanthauza kuti mayi ayenera kuchoka komwe akukhala kuti adzidyetse okha.


Amayi amatha kumawuluka atafumbatila mwana wake. Amatha kuwuluka chonchi mpaka mwana wake atakwanitsa pafupifupi sabata imodzi kapena ikakhala ndi mileme yodya zipatso mpaka mwanayo ali pafupifupi pa gawo limodzi mwa magawo atatu a kulemera kwawo. Akakulako, iwo amamusiya mwanayo aziwadikira pankhomo limodzi ndi ana ena onse a m'gululi, kuti azitenthesana pamene iwo apita kukasaka. M'mayi modzi wa milime amatha kutsalira kuti aziwasamala, koma usiku onse amayi amabwerabwera kuzayamwitsa ana awo mkaka ndi kumapitanso.

Pamene mayi abwerera kumalo kobadwila anaku iwo amazindikira mwana wake yemwe ali m'gulu la ana ena pakuzela kulira ndi fungo lake.




mwana wanga uyo...

Ayi, ndi wanga!



Kwa inu!



Ntchito 3:

Fananizani amayi ndi mwana wake

Kodi mungathe kufananiza ndi mawana wa mleme ndi amayi ake?
Tsatirani mizere kuti muwone kuti mwana ndiwa ndani!




7 Kukula ndikovuta

Ana a mileme ali ndi zambiri zoti aphunzire, ayenera kuphunzira; momwe akuwulukire ,



Mileme ina kupeza chakudya ayenera kuchithamangitsa ndikuchigwira, (Logan amayenera kumagwira njenjete ndi tizilombo tina, taganizirani kuyesa kumawuluka ndi njenjete yamoyo mkamwa mwanu kapena mutayigwira ndi phazi lanu),

momwe angapezere zakudya (kununkhiza zipatso zakupsa, mungu kapena timadzi tokoma tamumaluwa kapena kusaka nyama zamoyo).



ndipo mileme yambiri imayenera kuphunzira momwe angapangile ekolokeshoni! (Mileme yazipatso siitero koma ena onse amachita).

Zonsezi mumasabata 4 mpaka 6, yomwe ndi nthawi yokhazikika yomwe imatengera mileme wakhanda kuchoka malo obadwilako. Ana ena a mileme amaphunzira kuwulukira pogwira amayi awo, ndi kumakupiza mapiko awo mozondoka.

Akaphunzira kuwuluka palinso maluso ochulukirapo omwe amafunikira kuwaziwanso ...

Maluso ofunikira:

- kuzemba adani,
- momwe angapezere njira yobwerera kwawo,
- momwe angayendere komwe amakhala,
- komwe kuli malo ena omwe atha kumagonamo,
- momwe angasungile mphamvu zamuthuphi nthawi yomwe chakudya chili chosowa.



Chaka choyamba cha moyo wa mileme ndichovuta kwambiri, pali zambiri zoti ndiphunzire! Mwina ndingogonapo kaye! Usiku wabwino!

Kafotokozedwe ka mawu (mawu omwe taphunzira lero!)

Gesiteshoni - ndi nthawi yomwe imatengera mwana kukula m'mimba mwa mayi ake mpaka atakonzeka kubadwa. (Nthawi yomwe mayi ali ndi pakati.)

Matenite colone - gulu la mileme yaikazi yomwe imagona pamodzi pamene ili ndi pakati, kubereka komanso kuyang'anira ana awo.

Matenite - malo omwe mileme yaikazi imabisala pamene ali ndi pakati, pobereka komanso poyang'anira ana awo. Chisa cha amayi oyembekezera chiyenera kukhala chofunda, chotetezeka (ku zilombo kapena chisokonezo) komanso pafupi ndi malo abwino odyetserako ziweto.



Ndikukhulupirira kuti mwaphunzira
zambiri lero!

Tikuwonani sabata yamawa, kuti mudziwe
zonse za zowuluka zabwino kwambiri!

Musaiwale; mayankho azochitikazo
apezeka patsamba la Facebook la Bats
without Borders!